


Kwa inu!




## Ntchito 1:

# Kodi mungawerenge bwanji amayi ndi mileme ya ana pachithunzichi?

M'chisa cha mitengochi muli amayi ambiri ndi ana awo, akumakumbatirana mokoma ndi kutentha. Ndi amayi angati (maso akulu) ndi makanda (maso aang'ono) omwe mungawerenge?



Amayi = Ana  
13 = 13



Iyenera kukhala ntchito yovuta kwambiri kuti mileme ibereke. Mwana akabadwa amakhala wamkulu kwambiri poyerekeza ndi kukula kwa mayi ake.




"Logan anali 2.5 magalamu pamene anabadwa, sizingamveke zambiri kwa inu koma ndinangolemera magalamu 7 ndisanakhale ndi pakati. Iye anali akupitirira gawo limodzi mwa magawo atatu a kulemera kwanga kwanthawi zonse!"

"Ndinali ndi magalamu 50 pamene ndinabadwa, chimenecho chinali pafupifupi gawo limodzi mwa magawo asanu ndi limodzi a kulemera kwake kwa amayi anga (300 magalamu). Pamene ndinasiya kuyamwa ndinali nditalemera magalamu 135."



**Kwa inu!**



## Ntchito 2: Kulemera kwa mwana

Mungakonde kudziwa gawo la kulemera kwa amayi anu pomwe munabadwa.


Kuti muchite izi gawani kulemera kwa amayi anu (asanakhale ndi pakati) ndi kulemera kwanu pamene munabadwa. ( ndibwino mugwiritse ntchito ma kilogramu osati mapaundi). Kenako ikani yankho lanu pansu pa 1 mwachitsanzo ngati kulemera kwa amayi kugawidwa ndi kulemera kwa mwana = 19, chigawocho ndi 1\19th.

Ngati amayi anu sakukumbukira nacha chitsanzo:


Kulemera kwa amayi asanatenge mimba = 60Kg  
Kulemera kwa mwana pakubadwa = 3kg

**Yankho:**

$$\frac{1}{20}$$



Kwa inu!



## Ntchito 3:

# Fananizani amayi ndi mwana wake

Kodi mungathe kufananiza ndi mawana wa mleme ndi amayi ake?  
Tsatirani mizere kuti muwone kuti mwana ndiwa ndani!

